NYA_TTB_0941_20161107_**script**

Danieli : 11:1-14

Mutu : Kupitiliza kuona masomphenya a Danieli

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa 1 Yohane 1:18, akuti, "Tidziwa kuti yense Wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachimwa, koma iye Wobadwa kuchokera mwa Mulungu adzisunga yekha, ndipo woipayosamkhudza."

Mupologalamu yatha tinali kusanthulaDanieli 10:10-21, m'mene timaunika za m'thengawa Kumwamba. Ndipo lero pa Danieli 11:1-14, tipitiliza kuona masomphenya a Danieli.

Danieli 11

M'mbuyomu tidanena kuti ma chapter 10-12, akufotokonza za masomphenya amodzi. Ndipo lero chapter chino chikupitiliza kuonetsa masomphenya a m'mbuyomu. Tikunena kuti ichi ndichapter chomwe chikupereka pfundo zina zofunikira zomwe ziri m'masomphenya a fano la miyala lomwe likuimira maufumu anayi omwe ali m'chapter 2 ndi chapter 7. Ndiye tionanso chifukwa

chimene satana anatsekerezeramngelo Gabrieli kuti asakapereke yankho la pemphero lake.

Chinthu china chomwe ndichofunika kwambiri chomwe chapter chino chikuonetsa, ndi ulosi umene ukulumikizitsa Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano.Taonani kawiri-kawiri anthu ambiri akhala akunena kuti pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano pakhala popanda chinthu china chochitika, awa simaganizoolondola ayi.Chilungamo chake chikuti nthawi ya pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano ndiyo nthawi yomwe Israyeli anali pamasautso akulu, popeza ndiyo nthawi pomwe anasautsika kwambiri ndi Syria ndi Aigupto.Tikunena kuti pamene asirikari a mitundu ya anthu awiriwa anali kumenyana, iwowa anali kumenyerana m'dziko la Israeli kotero kuti Israyeli anasowa mtendere.

Ndiye tiyenera kudziwanso kuti nthawi ya pakati pa zipangano ziwirizi, ndiyo nthawi yomwe Antiokasi Epifane, amene anali kuimira wotsutsa Kristu, anali mkudza m'tsogolo.Tsono Antiokasi ndiye anabadwa m'banja la Seleusi, ndipo tidzamuzindikiradi pamene tipitiliza kusanthula chapter chino.Uyu, ndiye munthu

amene anazuzadi a Yuda, koposa falawo, Hamani, ngakhale Hilter.Iyeyu, akutchulidwa Nero m'mbiri ya a Yuda, amene akudziwikanso kuti ndiye ananyoza Mulungu kopambana.

Chapter chimenechi, chikuonetsanso kusiyana kwakukuru pakati pa mbiri (History) ndi ulosi.Ndiye muyenera kudziwa kuti nkhani yambiri m'bukuli inali ulosi, koma zambiri zinachitika kotero kuti pano ndimbiri yakale.

Tsono ulosi umene tiuonewu, ndiwo wokhwima kotero kuti anthu ambiri saumvetsa ayi.Ndikunena mau amenewa chifukwa anthu ambiri amakonda gawo lomwe ndi losangalatsa la ulosi, koma sakhala ndi chidwi chofufuza m'mau a Mulungu kuti apeze tanthauzo lake.Tere, chapter chino ndichomwechikupatseni mwayi wosanthula za ulosiwumwatsatane-tsatane.

Ndiye tikunena kuti ulosi uwu, ndiwo umene umangirire pakati pa ufumu wa Amedi-Peresiya ndi ufumu wa a Greek/Helene. Mwanjira ina tikunena kuti ulosi uwu, ndiwo umene ukuonetsa kusintha kwa ulamuliro wa dziko kuchoka ku maiko akulu-akulu Asia ndi kupita kuulamuliro wa ku Europe, kapena kuti kuchoka kuulamuliro wa kum'mawa kupita kuulamuliro wa kumadzulo.

Ulosi uwu, ndiwo wokhudza Israeli pamene kusinthaku kunali kuchitika.Pachifukwa chimenechi, Israyeli anabvutika kwambiri.

1. Ndipo ine chaka choyamba cha Dariyo m'Medi, ndinaukakumlimbikitsa ndi kumkhazikitsa.

Nkhani iyi, ikuchokera m'chapter 10, kotero kuti amene akulankhulayu ndiye mngelo wa Mulungu, amene ayenera kukhala Gabrieli. Ichi, chidachitika m'nthawi ya ulamuliro wa mfumu Dariyo pamene Danieli anali m'dzenje la mikango. Mukumbukira kuti Dariyo anayesetsa kuti aombole Danieli, koma sizinatheke chifukwa anali mumsampha wa lamulo lake lomwe. Koma adanena kwa Danieli 6:16, kuti, "Mulungu wako amene umtumikira kosalekeza, Iyeyuadzakulanditsa."

Tere pano m'chifukwa chake mngeloyu akunena kuti, "Ndinaukakumlimbikitsa ndi kumkhazikitsa."Kutanthauza kuti mngeloyuanadza kulimbikitsa Dariyo m'chikhulupiriro chomwe analinacho.Komanso mngelo yemweyo anatonthoza ndi kumuthandiza Danieli. Ichi, ndichifukwa chake Danieli adanena pa 6:22, kuti, "Mulungu wanga watumamthenga wake, natseka pakamwa pa mikango."

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndikokoma kuona dzanja la Ambuye pamene abale akutengapo gawo pantchito za mpingo wa Mulungu. Apa ndipo pamene tiyenera kulimbikitsa ganizo kapena ntchito zotere. Ndipo tiphunzira kuti pamene ife, tizindikira kuti ndi Ambuye amene akutsogoleramuntchitozothandiza mpingo, tiyenera kulimbikitsidwa kudalira pa Yehova ngakhale pamene tilikukumana ndi zobvuta.

2. Ndipo tsopano ndikufotokonzera choonadi. Taona, adzaukanso mafumu atatu m'Peresiya ndi yachinayi idzakhala yolemera ndithu yoposa onsewo; ndipo itadzilimbitsa yokha mwa kulemera kwake idzawautsa onse alimbane nawo ufumu wa Helene.

Tsopano mngelo wa Mulungu akumuuza Danieli za ulamuliro wa mafumu anayi ya Peresiya. Ndiye mngelo akumuuza Danieli kuti afuna kumuuza tanthauzo loona ndi momveka bwino za masomphenya ambuyo muja, a fano lalikuru ndi zirombo zinayi, zomwe zinali kuonetsedwa moipa.

Tere akunena kuti padzauka mafumu atatu, kupatula mfumu Dariyo popeza masomphenya awa, anali kuonetsedwa muulamuliro

wake.Mafumu amenewa ndiwo Koresi, Atazekisi ndi Ahaziwero, amene anakwatira Estere. Tsono Ahaziwero ndiye mwana waHistapes. Ndiye a Peresiya anali kuwalemekeza ndi mayina aulemu monga Koresi anali kutchulidwa tate, pamene Atazekisi (Kambasi) anali mbuye ndipo Dariyo ndiye anali kudziwika kuti wosonkhanitsa chuma.Tikunena kuti Dariyo ndiye anaika misonkhoikuru-ikuru pa anthu, pofuna kusonkhanitsa chuma chochuluka mwanjira imeneyi.Tsono mngelo akuti, pambuyo pa mafumu atatuwa, padzabwera mfumu amene, adzadziwika ndi kulemera kwake, koposa mafumu atatuwa.Mfumu uyu, ndi Zekisi, amene chuma chake a Greek anachitama kwambiri. Ichi, ndichuma chomwe anasonkhanitsa kuchokera kwa mafumu ena atatuwa.Ndiye ndi chuma chakechi, anakwanitsakulipira ndi kusamaliraasirikari oposa 800,000 omwe anaopseza nawo a Greek. Uyu, ndiye mfumu wotchuka m'mbiri ya a Greek, amene anali kuopseza kwambiri pakuturukiram'mabwalo ya a Greek.Koma akudziwikansokwambiri chifukwa cha momwe anachititsidwira manyazi ndi a Greek, motsogozedwa ndi Alexander.Apa, Zekisi anagonja kwa a Greek, pamene anali atagonjetsa molimba a Greek m'chaka cha 480 B.C.Pano ndipofunikanso kunena kuti utatha

ulamuliro wa Zekisi, anabweranso mafumu ena ambiri, koma yemwe akumveka ndi mfumu Zekisi chifukwa ndiye amene akukhudzana ndi kugwa kwa ufumu wa Peresiya, umene unakhudzanso a Yuda.

Ndiye nkhani ikunena kuti mbiri ya mfumu yolemerayi, ndiyo imene inakhudza Danieli chifukwa ndiye mfumu, amene amaoneka kuti chinali chotchingachakumangansokwa Kachisi. Koma patapita zaka makumi atatu, gulu loyamba la a Yuda atabwerera kwawo, mfumu yachinyamata yotchedwa Dariyo ndiyo imene inapitiliza ntchito yomanga Kachisi wa Mulungu. Iyi, ndiyo nkhani yomwe tikuipeza pa Ezra 6:7, imene ikuti, “Lekani ntchito iyi ya Mulungu, osaibvuta; kazembe wa a Yuda ndi akuru a Yuda amange nyumba iyi ya Mulungu pambuto pake.”

3. Ndipo idzauka mfumu yamphamvu, nidzachita ufumu ndi ulamuliro waukuru, nidzachita monga mwa chifuniro chake.

Pamene Danieli akukamba za mfumu yamphamvu, akunena za Alexander, the Great, amene anatenga ulamuliro wa a Greek /Helene, m’chaka cha 335 B.C. Ichi ndichaka chomwe anagonjetsa Peresiya nadzitengera ulamuliro wa dziko lonse lapansi. Tsono

ndikoyenera kunena kuti utatha ufumu wa Zekisi wa Peresiya, unadza ulamuliro wina, ufumu umenewu, utathyoledwa ndi Alexander.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti ufumu wa a Peresiya ndiwo unali wamphamvu padziko lonse lapnsi, kotero kuti pamene Alexander the Great, anagonjetsa Peresiya, analengeza kuti wagonjetsa dziko lapansi lonse.Apa, ndipo pamene Alexander, the Great anakhala pansi ndi kulira popeza panalibenso dziko lina lakuti aligonjetse.

Iyi, ndiyo mfumu yomwe ikutchulidwa kuti ndi mfumu yamphamvu yomwe “idzauka, nidzachita ufumu ndi ulamuliro waukuru, nidzachita monga mwa chifuniro chake.”Tsono mau akuti, adzachita monga mwa chifuniro chake, anakwanitsidwa pamene anagonjetsa maiko akum’mawa (Asia), ndipo anthu anayamba kumulambira ngati mulungu.Kutanthauza kuti mfumu Alexander anakhazikitsa malamulo ndi mphamvu monga Mulungu.

4. Ndipo pakuuka iye ufumu wake udzathyoledwa, nudzagawikira ku mphepo zinayi za mlengalenga; koma sadzaulandiraambumba yake akudza m’mbuyo, kapena

monga mwa ulamuliro wake anachita ufumu nawo; pakuti ufumu wake udzazulidwa, ukhale wa ena, si wa aja ayi.

Poyamba tiyeni titsindike kunena kuti Alexander the Great anali munthu wodziwa nkhondo kwambiri padziko lonse lapansi.Pachifukwa chimenechi, iye anali kuchita monga mwachifuniro chake.Mukumbukira tidanena kuti mfumuyuanadzikweza kotero kuti anali kulambiridwa ngati Mulungu.Mwachisoni kuti anafa ngati chitsiru.Tikunena kuti Alexander the Great anafa chifukwa cha mowa. Kutanthauza kuti chifuniro cha mtima wa munthu ndicho chimatsogolera munthu kuphompho. Ndipo mau a Mulungu pa Yesaya 57:17, akunena kuti, “Chifukwa cha kuipa kwakusirira kwake ndinakwiya ndi kumenya iye; ndinabisa nkhope yanga, ndipo ndinakwiya ndipo iye anankabe mokhota m’njira ya mtima wake.”

Tsono pamene Alexander anafa, ufumu wake unapitakwa anthu ena, popeza ana ake anali ataphedwa onse. Kutanthauza kuti chuma ndi ulemu wadziko lapansi ulibe ntchito ngati zitumikirachifuniro cha munthu. Tere tamvani kuti ufumu wake wonse, unagawikapanayi, kwanduna zake zomwe zinali kulamulira

zigawozinayi za ufumuwo. Taonani Kasanda anatenga ulamuliro wa chigawo cha Makedoniya, pamene Lisimas analamulira chigawo cha Asia (Turkey), pamene SeleukasNikata, analamulira Syria ndipo Pitoleme anatenga ulamuliro pa Aigupto.

Tsono chotsatira cha kugawikakwa ufumu uwu, chinali chakuti chikhalidwe ndi malamulo amene anakhazikitsidwasizinatsatidwe kotero kuti panalibe m'gwirizano pakati pa olamulirawa. Chotsatira chake chinali kumenyana pakati pawo ndiye chifukwa chogawikana, onsewa analanditsa ufumu wawo kwa a Roma.Kutsimikiza mau akuti zonse zapansi pano mzachabe, ndipo ndizosautsa mtima chabe.

5. Ndipo mfumu ya kumwera ndiye wina wa akalonga ake, idzamposa mphamvu, nidzakhala nawo ulamuliro; ulamuliro wake ndi ulamuliro waukuru.

Tsopano mngelo wasiya kukamba za Asia ndi Greece ndipo wayamba kukamba za ufumu wakum'mwera, Aigupto ndi ufumu wakumpoto, Syira, amene anali mumkangano ndi mafumu amene analowa m'malo mwa Alexander. Ndiye chifukwa chomwe wayamba kukamba za maikowa ndi chakuti ndiwoamene

anasowetsamtendere Yuda, popeza ndiye ali pakati pamaiko awiriwa. Ndiye pamene Baibulolikamba za kum'mwera, likunena za maiko amene ali kum'mwera kwa dziko la Israyeli. Ndipo pamene tiona kum'mwerakwa Israyeli tipeza dziko la Aigupto, kotero kuti tikamba zakuti PitolemeSoter ndiye amene anauka ngati mfumu ya mphamvu. Uyu ndiye anathyola Yuda pasabata, pamene anatenga mzinda wa Yerusalemu mwachinyengo monga bwezi. Seleukas mfumu ya Syria inasautsanso Yuda.Apa, ndipo pamene panadza ganizo lofunakuyanjanitsa mafumu awiriwa, koma zinali ngati kufuna kulumikizadongo ndi chitsulo monga muja zinali ndi fano la Nebukadnezara.Kutanthauza kuti sizinatheke kutero.

6. Ndipo pakutha zaka adzaphatikizanaiwo; ndi mwana wa mkazi wa mfumu ya kumweraadzafika kwa mfumu ya kumpoto, kupangana naye zoyenera; koma mkaziyosadzaisunga mphamvu ya dzanja lake; ngakhale mwamunayosadzaimika, ngakhale dzanja lake; koma mkaziyoadzaperekedwa, pamodzi ndi iwo adadza naye, ndi iye amene anambala ndi iye amene anamlimbitsa nthawi zija.

Mundime ino muli ganizo loyesakuthetsa nkhondo pakati pa ufumu wa kum'mwera wa Aigupto ndi ufumu wa kumpoto, wa Syria, ganizo limene linadzandi mfumu ya kum'mwera PitolemeFiladefas, amene anapereka mwana wake wamkazi, Berenice, kuti akwatiwe ndi mfumu Antiokansi ya Syria, amene anathetsa ukwati wake ndi mkazi wake Wamkulu. Mafumu awa ndi amene analowa m'malo mwa PitolemeSoterwa ku Aigupto ndi SelukasNikata, wa ku Syria. Awa, analowa pamgwirizanowaukwati ndi cholinga chakuti pakhale mtendere pakati pawo.

Koma taonani mundimeyi muli mau akuti, "koma mkazi sadzaisunga mphamvu ya dzanja lake; ngakhale mwamunayosadzaimika."Kutanthauza kuti mkazi uyu, sadzalamuliramuufumu uwu, monga mwacholinga cha ukwatiwu, popeza atate wake, Pitoleme, amene anampereka kuukwati anafa, banjalilisanakhazikike, kotero kuti mfumu ya Syria inabwererana ndi mkazi wake wakale. Koma mkazi wa Antiokasi, anapha mwamuna wake pamodzi ndi mkazi waku Aigupto uja, pamodzi ndi mwana wawo. Kutsimikiza ulosi wakuti mkazi sadzaisunga mphamvu ndipo mwamuna sadzaimika.

7. Koma apopophukira mizu yake adzauka wina m'malo mwake, ndiye adzafika kulimbana nalokhamu la nkhondo, nadzalowam'linga la mfumu ya kumpoto, nadzachitamolimbana nawo nadzawalaka;

Pano pali ganizo lakuti munthu wina adzaphuka, wochokera ku banja la Berenice, mkazi uja wa ku Aigupto. Uyu, ndi mlongo wake amene adzathira nkhondo ndi cholinga chofuna kubwezera imfa ya mlongowakeyo. Ndiye pamene PitolemeEuergetes anamva za kuchotsedwa kuukwatikwamlongo wake, anathamanga ndi asirikari a nkhondo, koma mlongowakeyo pamodzi ndi mwana wake anali ataphedwa kale. Apa, ndipo pamene anaganiza zotenga ulamuliro wa Syria pamodzi ndi linga lomwe linali padoko la Antiokeya.

8. Ndi milungu yawo yomwe, pamodzi ndi akalonga awo, ndi zipangizo zawo zofunika za siliva ndi golidi adzazitenga kumka nazo ndende ku Aigupto; ndi zaka zake zidzaposa za mfumu ya kumpoto.
9. Ndipo adzalowam'ufumuwa mfumu ya kum'mwera, koma adzabwera m'dziko lake lake.

Tsono PitolemeFiladefas analamulira Syria nthawi yaitari kusiyana ndi mafumu awo, koma anaitanidwa kubwerera kwawo chifukwa chofuna kukasungitsa mtendere m'dziko lake. Ndiye pakubwerera kwawo, anatengako chuma ndi akapolo ambiri. Tsono taonani pamene mfumu Callinicuswa Syria anaona kuti chuma ndi anthu ake zinatengedwa kupita ku Aigupto, anayesera kukathira nkhondo ku Aigupto, koma anabwezedwa. Tere apa, tikuphunzira kuti mtendere wosadarikaumatheramkukhetsa mwazi.

10. Ndi ana ake adzachita nkhondo, nadzamemeza makamu a nkhondo akuru, ochuruka amene adzalowa nadzasefukira, nadzapita; ndipo adzabwerera, nadzachita nkhondo mpaka linga lake.

Awa, ndiwo ana aCallinicus, mfumu ya Syria, ufumu wa kumpoto, amene anaphedwa. Ndiye pachifukwa cha imfa yake, ana awiriwa anapsa mtima kotero kuti anasonkhanitsa asirikari awo ndi cholinga chokabwezera nkhondo Pitelomewa Aigupto popeza ndiye anayamba kukathira nkhondo Syria chifukwa cha imfa ya mlongo wake.Iwowa amafunitsitsa akalandedziko ndi chuma chomwe atate wawo analandidwa pankhondo ya mfumu ya Aigupto.

Ndiye titsirize ndi mau akuti nkhondo iyi, inayambika ndi atate wawo amene anafa atagwa pa kavalo wake.Tere, ndiyo nkhondo yomwe inapitilizidwa ndi ana ake awiri; SeleucusCeraunusa ndi Antiokasi the Great, kufikira mwana woyambayuatafa. Antiokasi anamenya nkhondo yonseyi yekha, amene anakwanitsakulanda ufumu onse wa Aigupto. Tsono chimene ndifuna tione ndi chakuti, pamene nkhondo zonsezi zinali kuchitika, Israeli anali kuthawira uku ndi uku, kutsatira mbali yomwe ikuonetsa kupambana.Lero anthu ena akuchita chomwechi, kuti akuona ngati kuti satana akupambana, kotero kuti asiya kutsatira Mulungu.kodi inu ndinu m'modzi wa anthu amenewa?

Lero tilekeza pano ndipo tinali kusanthula Danieli 11:1-14, momwe timapitiliza kuona masomphenya a Danieli.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!